Kodi Yesu Khristu Ndi Ndani? (Gawo 2)

Nkhaniyi yachokera m'mutu 4 m'buku lakuti, *Kodi Baibulo Limaphunzitsa Chiyani Kwenikweni?* lomwe likupezeka pa jw.org.

ZIMENE MUYENERA KUCHITA: Ganizirani mozama zimene mumakhulupirira ndiponso zifukwa zake, fufuzani zimene Baibulo limaphunzitsa, kenako ganizirani mmene mungafotokozere ena zimene mumakhulupirirazo.



KODI YESU NDI WAMKULU MOFANANA NDI MULUNGU?

1 GANIZIRANI MOZAMA ZIMENE MUMAKHULUPIRIRA

N'chifukwa chiyani ena angayankhe kuti inde?

N'chifukwa chiyani ena angayankhe kuti ayi?

Kodi **inuyo** mumakhulupirira zotani?

Nanga n'chifukwa chiyani mumakhulupirira zimenezo?

www.jw.org © 2014 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

2 FUFUZANI ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA

Yesu ali ndi chiyambi pamene Mulungu alibe chiyambi.

(Werengani mutu 4 m'buku lakuti *Baibulo Limaphunzitsa Chiyani,* ndime 10 mpaka 12.)

Werengani Akolose 1:15, 16.

N'chifukwa chiyani zili zoyenera kuti Baibulo limati Yesu ndi "woyamba kubadwa wa **chilengedwe** chonse"?

Werengani Salimo 90:2.

Kodi Yehova Mulungu ali ndi chiyambi?



Ngati Yesu ali wamkulu mofanana ndi Mulungu, n'chifukwa chiyani anatchula Mulunguyo kuti Atate ake osati mchimwene wake?

www.jw.org © 2014 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

Yesu anaphunzitsa kuti Mulungu ndi wamkulu kuposa iyeyo.

(Werengani mutu 4 m'buku lakuti *Baibulo Limaphunzitsa Chiyani,* ndime 12 mpaka 14.)

Werengani Yohane 14:28.

Malinga ndi vesili, kodi Yesu ankaganiza kuti ndi wamkulu ngati Mulungu?

Werengani Yohane 14:31.

Kodi zimene Yesu anachita pomvera malamulo a Mulungu, zinasonyeza bwanji kuti sanali wamkulu mofanana ndi Mulungu?

N'chiyani chimakupangitsani kutsimikiza kuti Yesu si Mulungu?

www.jw.org © 2014 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

3 FOTOKOZANI ZIMENE MUMAKHULUPIRIRA

WINA AKANENA KUTI . . .

Yesu anachokera kumwamba, choncho ayenera kukhala Mulungu.

MUNGAYANKHE KUTI . . .

N'zoona kuti Yesu ankakhala kumwamba asanabwere padziko pano. Koma ndikukhulupirira kuti zimenezi sizingapangitse kuti akhale wamkulu mofanana ndi Mulungu chifukwa **. . .**

_____

_____

Kodi mungawerenge lemba liti kuti mumuthandize?

_____

Kodi mungafotokoze bwanji vesilo pomuthandiza malinga ndi zimene amakhulupirirazo?

_____

WINA AKANENA KUTI . . .

Yesu ananena kuti iyeyo ndi Mulungu.

MUNGAYANKHE KUTI . . .

Anthu ambiri akhoza kuganiza choncho. Koma ine sindimakhulupirira zimenezo chifukwa . . .

_____

_____

Kodi mungawerenge lemba liti kuti mumuthandize?

_____

Kodi mungafotokoze bwanji vesilo pomuthandiza malinga ndi zimene amakhulupirirazo?

_____

www.jw.org © 2014 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania